

# UTHENGA WABWINO WA CHOONADI


MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO  
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

## UTHENGA WABWINO

Kwala kochokera kumwamba kunawala usiku pamene gulu lalikulu la angelo akumwamba linadzaza thambo lonse. Kuimba kwa angelo kunamveka mwanthetemya pamene amalemekeza Mulu-nku Wamphamvuzonse. Iwo amaimba mwamphamvu ndi mokondwera kuti, "Ulemerero ukhale kwa Mulungu Ku-mwambawamba, ndi mtendere pansi pano mwa anthu amene akondwera nao." (Luka 2:14).

Zikanakhala zokoma kuona zinthu izi zodabwitsa zimene zinachitika zaka 2,000 zapitazo. Kodi ndi chiyani chimene chinapangitsa amithenga a Mulungu kuti abwere ku dziko lino lapansi, atanya-mula uthenga wa mtendere ndi wa nkhanzi zabwino kwa anthu? Kumeneku kunali kubadwa kwa Yesu Khristu, mwanza wa Mulungu wamoyo.

Patapita zaka zokwana 30 chichitikireni izi, Yohane Mbatizi ataona Yesu anati, "Onani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo lake la dziko lapansi!" (Yohane 1:29). Nzasadabwita kuti angelo anaimba mokondwera pa kubwera kwa Mpulumutsi Wolonjezedwa uja amene anabwera



*"Monga madzi ozizira  
kwa munthu woto pa,  
momwemo mau  
abwino akuchokera  
kudzikko lakutali."*

*Miyambo 25:25*

kudzaombola mtundu wa anthu komanso kuphwanya mphamvu ya uchimo ndi imfa m'moyo wao. Uchimo ukuchulukirachulukira m'dziko lino ndipo umabewereka chisoni, kutsutsika, undekha, ukapolo komanso kusowa chiyembekezo. Miyoyo ya anthu komanso mabanja akuonongeka ndi mphamvu ya mdierekezi. Koma

tiyamike Mulungu kuti tili ndi Uthenga Wabwino! Kudzera mu mphamvu ya Yesu Khristu, timapezabe mtendere kwa anthu ngakhale panopa pamene tili pakati pa dziko lovutali. Kudzera mwa Yesu Khristu mphamvu ya uchimo ingathe kuonongedwa ndipo chiyembekezo ndiponso moyo zingathe kulowa mmalo mwa mtima wosweka ndi imfa.

"Monga madzi ozizira kwa munthu wotopa, momwemo mau abwino akuchokera kudzikko lakutali." (Miyambo 25:25). Zimakhala zosangalatsa kulandira Uthenga Wabwino patsiku la msautso ndi la mavuto. Pali uthenga wabwino kwa moyo uliwonse umene ukusautsika. Uthenga umenewu ukupezeka mu uthenga wabwino wa Yesu Khristu. Uthenga Wabwino ndiwo wakuti Yesu Khristu anabwera kudzachita zimene ifeyo sitikanatha kudzichitira patokha. Yesu Khristu akuchitabe zodabwitsa m'miyoyo ya anthu pobwezeretsa ndi kuchiritsa iwo amene ndi odwala ku uzi-mu. Pamene palibe populumukira, Yesu amapereka njira. Yesu amapangitsa zosatheka kuti zikhale zotheka.

(Zapitirira pa tsamba 1)

Mau a Mkonzi

Tsamba 3

Kusanthula Baibulo—  
Choonadi: Santhulan  
Mau a Mulungu monga  
anachitira a ku Berea

Tsamba 4

Kodi choonadi ndi  
chiyani: Pali choonadi  
chimodzi chimene  
chimapezeka mwa  
Khristu yekha basi  
Tsamba 5

Mafanso ndi Mayankho:  
Kodi kuhala oona mti-  
ma ndi kokwanira. Kodi  
zili ndi kanthu zimene  
ndimakhlupirira?  
Tsamba 7

Mau a pa Nyengo yake:  
Ndinu a mtengo wake  
kuposa mpheta zambiri.

Tsamba 8

# zimene BAIBULO limaphunzitsa za...

## **Mau a Mulungu**

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

## **Ubale wa Chikondi**

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

## **Kulapa**

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

## **Kubadwa mwatsopano**

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

## **Kupulumuka ku uchimo**

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

## **Chidzalo cha Mzimu Woyeria**

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

## **Chilero**

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

## **Ufumu wa Mulungu**

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

## **Mpingo**

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akor. 1:18

## **Umodzi**

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

## **Maskaramenti**

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

## **Machiritso**

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

## **Chilero cha Banja**

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

## **Chikhaliidwe cha pakati pa anthu ena**

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

## **Masiku omaliza**

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

## **Kukhala mwa mtendere**

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

## **Kupembedza**

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

## **Kulalikira Uthenga Wabwino**

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba I)

Ulaliki woyamba kulembedwa umene Yesu anaulalikira umatambasula Uthenga Wabwino: "Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, chifukwa chake lye ana-nandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: anandituma Ine kula-likira am'nsinga mamasulidwe, ndi akhungu kuti apenyanso, kutulutsa ndi ufulu ophwanyika, kulalikira chaka chosankhika cha Ambuye" (Luka 4:18-19).

Yesu amakukondani ndipo uthenga wabwino ndi ofunikirabe ngakhale lero. Yesu akanakhululukirabe ochimwa ndipo akanachirtsabe odwala. Yesu adzatumikira kwa munthu aliyense amene ali wosakondwa, wosautsika mumtima, wakhungu, kapena wopwetekedwa. Chofunika ndicho kungotsekula mtima wanu basi ndi kulilira kwa Ambuye. lye akuyembekezera kuti amve kulira kwanu.

"Mukani kudziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse" (Marko 16:15). Uthenga Wabwino waulemerero ndiwo uthenga wa chiyembekezo kwa anthu onse kulikonse, a chikhaliidwe chilichonse ndi mtundu uliwonse. Pamene tikuzindikira kuti uthenga uwu wabwino ndiwo weni-weni, tiyeni tikhale wokhulupirika powulalikira kwa iwo amene timakhala nawo koma ali wosautsika mumtima. Sizitengera zimene ife tingachite, koma zimene Yesu akhoza kuchita ndipo zimene angachite. Ulemerero ukhala kwa Mulungu chifukwa cha Uthenga Wabwino.

-mws

## **UTHENGA WABWINO WA CHONADI**

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoona za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiro. Amaphunzitsa chipulumuto ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maomboledwe ya mwa Yesu Christu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyeria kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, twongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chilero choonekera pa gavo ililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

## **KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI**

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timesindikiza miyezi itatu ililyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa [email](mailto:email), pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa [www.thegospeltruth.us](http://www.thegospeltruth.us). Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma [email](mailto:email) a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mknzi.

## **KUTI MUTIPEZA**

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizida mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

# Mau a Nkonzi



"Koma ngatinso Uthenga Wabwino wathu uphimbika, uphimbika mwa iwo akutayika; mwa amene mulungu wa nthawi yino ya pansi pano unachitsitsa khungu maganizo ao a osakhulupirira, kuti chiwalitsiro cha Uthenga Wabwino wa ulemerero wa Khristu, amene ali chithunzithunzi cha Mulungu, chisawawalire. Pakuti tilalikira si za ife tokha, koma Yesu Khristu Ambuye, ndi ife tokha akapolo anu, chifukwa cha Khristu."

(2 Akorinto 4:3-5).

Tikukhala mu nyengo imene yachititsidwa khungu osati ndi zikhumbitso za thupi komanso ndi zikhazi-kitso za zipembedzo. Ndikadakonda aliyense padzikoto atadiwiya ndi kumvetsetsa za mtendere umene umapezeko mwa Yesu Khristu. Mbusa aliyense kapena mpingo umene umalalikira za iwo wokha basi ndi wa chinyengo. Mu mphamvu zathu ndi kuthekera kwathu, palibe chimene tingachite pofuna kuti tipulumutse dziko lotayikali. Zimene tingatthe kuchita ndiko kuwalozera anthu kwa Mpulumutsi – osati ndi mau athu, koma ndi kuwala kumene kumabwera mwa ife kuchokera kwa Khristu amene amakhala mwa ife.

Ndikadakonda kuti kuwala kwa ulemerero kwa uthenga wabwino kuunikire mowala ndithu mu nyengo ino imene ili ya mdima. Kudzera mu zaka zambiri zotumikira pa dziko lino, ndazindikira kufunikira ko-yambitsa mautumiki ku maiko akutali kuti nawonso adziwe choonadi cha Mau. Sikuti ndikufuna kupeza anthu ambiri onditsatira kapena kuti wina wake alowe m'gulu lathu. Ndikufuna kuti anthu aphunzitsi-dwe ndi kulimbikitsidwa kukhala monga mpingo mu dera lao. Umodzi umabwera pamene anthu ayenda mu choonadi, koma potsogozedwa ndi Mzimu Woyeria.

Myezi ingapo yapitayi ndili ku Kenya kumene ndinalalikira uthenga wachidule, mbusa wina wochokera ku mpingo wina kumeneko anandiuza kuti, "Ndinadalitsika ndi ulaliki wanu." Kenaka anandiuza kuti atumiki ambiri amene amalalikira amafuna kuti anthu adziwayamikira. Palibe ufulu kapena mtendere weniweni ngati utsatira munthu kapena chipembedzo. Ndivomere kuti chipembedzo komanso moyo wokonda zadziko pakati pa akhristu zimandilemetsa kwambiri. Komanso panthawi yomwe ino, ndiku-lengeza mosaona chikondi changa pa Mulungu, pa choonadi ndi pa ana ake onse. Mtima wanga ukulili-ra ochimwa, anthu achiphamaso ndi amene abwerera mmbuyo kuti apeze kukwanirtsidwa. Izi sizipeze-ka mynymba ya mapemphero kapena potsatira njira yabwino yachipembedzo. Izi zimapezeko pamene munthu wadziperekwa kwathunthu kwa Yesu Khristu komanso potsata mosakamizidwa njira yopapati-za, yachimwemwe, yodzikhuthula, yokonda Baibulo imene imatsogolera ku moyo wosatha.

Ndi chokhumba cha mkazi wanga komanso cha ine mwini kuti tidzikugawiranu kudzera mmau olembe-dwa mu kalatayi zina mwa mfundu zoona zopezeko mmalemba zimene zikhoza kuthandiza mitima yoona kuti ikhazikike mmau. Tidzisindikiza pafupipafupi monga mmene Ambuye angatipatsire nthawi komanso kutiululira. Tidzakondwa mutatikumbukira m'mapemphero kuti ntchito iyi imene tangoyamba kuyichita ikakhale yopambana kuuzimu.

Tiyeni tonse tipempherere mdalitso wa Mulungu pa kukumana kwathu kulikonse m'nyengo ino. Muli mphamvu mu pemphero, ndipo ndikuyembekeza kudzaona mapiri ena akusalazidwa ndi mphamvu ya Mulungu.

-Michael W. Smith

Zambiri Zili pa  
INTANETI

Mukafuna kutipeza


pa intaneti, mulembe

[www.thegospeltruth.us](http://www.thegospeltruth.us)

kuti mudzilandira makalata

athu kapenango kuti muone

makalata akale.



## KUSANTHULA MAU A MULUNGU

**PEZANI NDIME YOYAMBIRA**  
Pezani ndime kapena buku la m'baibulo limene mukufuna kusanthula. Mabuku anai a Uthenga Wabwino, Yakobo, Tito, 1 Petro ndi 1 Yohane onse ndi abwino kwa anthu oyamba kumene.

**MUYAMBE NDI PEMPHERO**  
Mupemphere kuti Mulungu akupatseni nzeru, chitsogozo ndi kumvetsetsa. Pamene mukupemphera zindikiranu kuti mukusanthula Mau amene Mulungu anachita kuwauzira ndi mpweya wake. "Potsegulira mau anu paunikira; kuzindikiritsa opusa." (Salmo 119:130)

**WERENGANI NDIME YONSE**  
Ziphunzitso zambiri zabodza zagona pa kungochonyotsolapo ndime zingapo mwachidule zimene sizigwirizana ndi nkhanu yonse. Nkofunika kuwerenga ndime yonse kuti mumvetsetse bwino nkhanayo.

**MUPEZE MFUNDO ZENIZENI ZA NKHANIYO**  
Nkhani yonse tuyiduledule m'mavesi ndi kusanthula ndime iliyonse kuti mupeze tanthauzo lenileni. Muone ngati pali mau ofunika kuwamasulira kapena ndime zina zimene zikulongsolera bwino nkhanayo. Mudzilemba zimene mwapezazo.

**MFUNDO ZOTHANDIZA PA MOYO UNO**  
Mulole kuti Mau a Mulungu akulankhulenji mwapadera. Kodi ndimeyi ikunena chiyani ku moyo wanga?

**"MUKHALE AKUCHITA MAU"**  
Tsiku ndi tsiku mudzichita zimene Mau a Mulungu akunena. "Mau a Khristu akhalise mwa inu." (Akolose 3:16)

# KALOZERA POSANTHULA MAU A MULUNGU

## MUTU—CHOONADI

### Mau a Mulungu:

Yohane 18:37-38 Pamenepo Pilato anati kwa Iye, Nanga kodi ndiwe Mfumu? Yesu anayankha, Munena kuti ndine Mfumu. Ndinabadwira ichi Ine, ndipo ndinadzera ichi kudza kudzikzo lapansi, kuti ndikachite umboni ndi choonadi. Yense wakukhala mwa choonadi amva mau anga. Pilato ananena kwa Iye, Choonadi nchiyani? Ndipo pamene adanena ichi, anatulukiranso kwa Ayudawo, nanena nao, Ine sindipeza konse chifukwa mwa Iye.

**Tanthauzo la Choonadi:** *Icho chimene chili molingana ndi mfundo kapena zenizeni za nkhani; zolondola, ochita molunjika, zabwino, ochita moona, okhulupirika.*

Kuchokera ku mau a chi Griki akuti, "kusabisa".

### 1. Yesu ndiye Choonadi

- A. Yohane 1:14 Mau (Yesu) anasandulika thupi – wodzaza ndi chisomo ndi choonadi.
- B. Yohane 1:17 Chisomo ndi choonadi zinabwera ndi Yesu.
- C. Yohane 14:6 Yesu ndiye njira choonadi ndi moyo.
- D. Aefeso 14:6 Choonadi chili mwa Yesu.

### 2. Mau a Mulungu ndiye Choonadi

- A. Yohane 17:17-19 Mau a Mulungu ndiye Choonadi.
- B. 2 Timoteo 2:15 Santhulani ndi kugawa moyenera Mau.
- C. 2 Atesalonika 2:10 Munthu akonde choonadi kuti apulumutsidwe.

### 3. Mzimu wa Choonadi ndi Kupembedza

- A. Yohane 16:13 Mzimu Woyeria adzakutsogolerani ku choonadi chonse.
- B. Yohane 4:22-24 Mupembedze mu Mzimu ndi mu Choonadi.

### 4. Choonadi sichisintha ndipo ndi Chamuyaya

- A. Yesaya 40:8 Mau a Mulungu adzakhala mpaka kalekale.

- B. Salmo 100:5 Choonadi chikhalapo ku mibadwomibadwo.
- C. Luka 21:33 Mau a Khristu sadzatha.

### 5. Phindu la Choonadi

- A. Yohane 8:32 Choonadi chimamasula.
- B. Yohane 3:19-21 Choonadi chimaulula ndi kubweretsa kuwala.
- C. 1 Petro 1:22-23 Miyoyo yathu imayeretse-dwa pomvera choonadi.

### 6. Kuchoka pa Choonadi

- A. 2 Timoteo 4:1-4 Anthu adzasiya kutchera makutu awo ku choonadi.
- B. 2 Timoteo 2:16-18 Anthu amalakwa pokhudzana ndi choonadi.

### 7. Aphunzitsi onyenga

- A. 2 Petro 2:1-2 Padzakhala aphunzitsi onyenga pakati panu.
- B. Mateyu 15:9 Iwo amaphunzitsa kuchokera ku ziphunzitso za malamulo a anthu.
- C. Tito 1:14 Musawamvere.
- D. 1 Timoteo 6:3-5 Muchoke kwa aphunzitsi onyenga.

### 8. Chilango cha iwo amene samvera Choonadi

- A. Aroma 2:8-9 Mazunzo ndi masautso.
- B. 2 Atesalonika 1:8 Kubwezera.

### 9. Mpingo

- A. 1 Timoteo 3:15 Mchirikizo ndi pokhazikika pa choonadi.
- B. Zekariya 8:3 Ziyoni (Mpingo) udzatchedwa mzinda wa choonadi.

### 10. Zobetchera

- A. Miyambo 23:23 Gulani choonadi ndipo musachigulitse.
- B. 1 Yohane 1:6 Muchite choonadi posunga malamulo a Mulungu.
- C. Aefeso 6:14 Muime nji pa choonadi.

**Pemphero:** "Munditsogolere m'choonadi chanu, ndipo mundiphunzitse; pakuti Inu ndinu Mulungu wa chipulumutso changa; Inu ndiku-yembekezerani tsiku lonseli." - Salmo 25:5

# KODI CHOONADI NDI CHIYANI?

(Tsatanetsatane wa mau othandizira pa kusanthula kwa Mau Mulungu)

## "KODI CHOONADI NDI CHIYANI?"

Pilato anamufunsa Yesu funsoli pamene Yesuyo amaweruzidwa. Funsoli limafunsidwanso lero pamene anthu ali kalikiliki padzikio lonse kufuna mayankho a moyo wathuwu komanso mavuto ake. Atumiki ambiri, mipingi komanso anthu a ziphunzitso ndi zikhulu-piriro zosiyanasiyana amanena kuti 'ali ndi choonadi.' Nanga ndi zotheka bwani kuti maganizo ndi malingaliro osiyanasiyana amene onsewo ali olondola.

## PALI CHOONADI CHIMODZI CHOKHA

Zoona zake zenizeni ndizo zakuti pali choonadi chimodzi chokha basi, ndipo choonadi chimenechi chimapezeka mwa Yesu yekha basi. Yesu ndiye choonadi. Mau a Mulungu anasandulika thupi nakhala pakati pathu kuti atiunikire, awulule uchimo, aonetsera ndi kuphunzitsa zoona zenizeni za chiyero ndi kumasulidwa ku uchimo, ndi kupangitsa kuti tidziwe zenizeni za moyo wa mtendere umene umapezeka mu ubale wathu ndi Mulungu Atate.

## CHOONADI SICHISINTHA

Mulungu anatumiza Mzimu Woyera kuti atsogolere anthu mwaumunthu aliyense payekhapayekha mu njira ya choonadi. Choonadi chimaposa maganizo, kumene tachokera, mbiri ya mpingo, chikhaliidwe, mtundu ndi chikhulupiriro. Choonadi cha Mau a Mulungu sichisinthia kuchokera ku mbadwo umodzi kupita ku mbadwo unzake koma chikadali cholondola ndipo chimaperekira yankho ku moyo wosatha mu dziko lino limene lili lochimwa. Ziphunzitso komanso mbiri ya mpingo zimabwera ndi kupita, koma choonadi ndi chamuyaya ndi chosasintsha. Choonadi sichtengera zimene timaganiza ndi zimene timakumana nazo. Mau a Mulungu amafikira kwa anthu a mtundu uliwonse ndiponso ndi ofunkira kwa wina aliyense. Mzimu wa Mulungu sudzatitengera kumene kuli kotsutsana ndi choonadi cha Mau a Mulungu.

## CHOONADI CHIMAMASULA

Choonadi chimaunikira komanso chimamasula. Zikhulupiriro ndi zipembedzo za anthu zimabweretsa ukapolo ndi chisokonezo. Chifukwa chakuti pali ziphunzitso zosiyanasiyana ndi mipingi yochuluka, izi sizitanthauza kuti palibe choonadi. Choonadi

chimenechi chimapezeka mwa Khristu, chimalembedwa mu Baibulo ndipo chimatsimikizidwa ndi Mzimu Woyera. Choonadi cha Mulungu sichingathe kuwonjezeredwa kapena kuchotse-redwa chifukwa choti Abusa afuna, kapena chifukwa a bishopu ena kaya mtsogoleri wampingo wanena. Mau a Mulungu amaima paokha ngati choonadi. Malemba paokha ndi wokwanira. Anthu enieni a Mulungu amaperekira ulemu ndi kulemekeza Mau a Mulungu ngati choonadi ndipo amapondereza chikhulupiriro chilichonse ndi zikhulupiriro zonse za anthu.

## MAU ANASANDULIKA THUPI



Anthu ambiri mu dziko lino amanena kuti amakulupirira Khristu, koma amakana choonadi cha Mau a Mulungu ndi kutanthauzira kwake. Anthu ena amayesetsa kusianitsa pakati pa kusiyana kwa ziphunzitso za Baibulo ndi za Yesu. Choonadi chake ndicho chakuti izi ndi zimodzi ndiponso zofanana. Pamene wina akana gawo limodzi la chiphunzitso cha Chipangano Chatsopano, iyeyo akukana Khristu mwini.

## KANANI ANENERI ONYENGA

Mu mbiri ya mpingo woyamba, munali aphunzitsi onyenga komanso masiku ano tili nawo – atumiki amene amanena kuti ndi a Yesu koma saphunzitsa chiyero cha choonadi. Iwo amaphunzitsa choona chimene amangochilanhkula basi ndipo izi zimalimbikitsa moyo wa uchimo komanso ntchito zathupi pofuna kukopa anthu ochuluka. Kawirikawiri chinyengo chimapezeka mu mpingo ndiponso pakati pa atumiki amene amaphunzitsa choonadi. Nkosavuta kuzindikira bodza lenileni kusiyana ndi kuzindikira bodza limene laphatikizidwa ndi choonadi. Tiyeni tisaonenjezere kapena kuchotsapo pa izo zimene zalembedwa m'Mau a Mulungu.

## CHOKANI PAKATI PA MIPATUKO

M'masiku ano otsizira, anthu ambiri akuchoka pa choonadi cha Mau a Mulungu komabe akukhala ndi umboni wa moyo wabwino. Malemba amaphunzitsa anthu enieni a Mulungu kuti asadziphatizike ndi magulu oterewa ndipo achokepo pa

(Zapitirira pa tsamba 6)

chiyanjano cha atumiki oterewa. Kumwamba kukuyitana anthu okhulupirika ndi oyera, koma ku gehena kukuyitana anthu onse amene amakana choonadi chonse.

#### **MZIMU WOYERA AMACHITIRA UMBONI ZA MAU**

Ndikoyenera kuti mwana aliyense wa Mulungu adzadzidwe ndi Mzimu Woyerwa ndi kumalingalira pa Mau a Mulungu. Mzimu Woyerwa adzakhala okhulupirika kwa munthu aliyense amene ali olungama ndi oona mtima pa choonadi. Anthu amakhala pa milingo yosiyanasiyana pa kamvetsedwe kawo ka choonadi. Chifukwa chake, anthu osiyana amavomerezanzo zinthu mosiyana. Vuto limakhalapo pamene munthu sasamalira zimene Mzimu akumutsutsa komanso Malemba. Chinyengo chimalowa ndipo anthu amatsimikizika za mmene akuonera za choonadi. Kukhala oona mtima pakokha sikupangitsa kuti munthu akhale wovomerezeka pamaso pa Mulungu, koma kukhulupirika ndi chilungamo, kuphatikizapo choonadi. Izi zimapangitsa kuti munthu akhale moyo wovomerezeka pamaso pa Mulungu. Mukhale wokhulupirika ku Mau a Mulungu ndipo mudziwe kuti Mzimu Woyerwa sadzatsogolera mosemaphana ndi Mau a Mulungu.

#### **KODI MUKUYENDA M'CHOONADI?**

Mpingo wa Mulungu ndiwo munthu komanso gulu la anthu oyanjana pamodzi amene alola kuti choonadi chikhale chotsogolera moyo wao. Ziyoni, mpingo wa Mulungu, uyenera kukhala mzinda wa choonadi. Si dzina chabe loikidwa pamphuthu ya chitseko cha nyumba yopempherera koma kukhala mmoyo weniweni wa choonadi. Mulole kuwala kwa choonadi kuti kuunikire mowala kwambiri mu mtima mwanu.

-mws



#### ***Khalani Akuchita***

*"Khalani akuchita mau, osati akumva okha,  
ndi kudzinyenga nokha.  
Pakuti ngati munthu ali wakumva mau,  
wosati wakuchita,  
iyeyu afanana ndi munthu wakuyang'anira  
nkhope yake ya chibadwidwe chake  
m'kalirole;  
pakuti wadziyang'anira yekha,  
nachoka, naiwala pompaja nali wotani.  
Koma iye wakupenyerera m'lamulo langwiro,  
ndilo laufulu, natero chipenyerere,  
ameneyo, posakhala wakumva wakuiwala,  
komatu wakuchita ntchito,  
adzakhala wodala m'kuchita kwake."*

*Yakobo 1:22-25*

# Mafunso

## ndi Mayankho




(Izi zalembedwazi ndi zina pang'ono mwa zimene analenba malemu Mbale Ostis Wilson Jr.)

**Funso:** Nthawi zambiri timamva kuti zilibé kanthu zimene anthu amakhulupirira bolani ngati akuchita moona mtima. Kodi izi ndi zoona?

**Yankho:** AYI, IZI SI ZOONA, ndipo ndi zotheka kuti munthu akhoza kuchita zinthu moona mtima koma akulakwitsa monga mmene angakhulupirikire pa chimene chili choona. Mau a Mulungu amanena kuti, "... Mulungu anakusankhani inu kuyambira pachiyambi, mulandire chipulumutso mwa chiyeretso cha Mzimu ndi chikhulupiriro cha choonadi:" 2 Atesalonika 2:13. Apa tikuona kuti "chikhulupiriro cha choonadi" ndi gawo lofunikira kwambiri pa njira komanso chikonzero chimene Mulungu watiyikira kuti tipeze chipulumutso. 2 Timoteo 4:3-4 akunena kuti, "Pakuti idzafika nthawi imene sadzalola chiphunzitso cholamtsa; komatu poyabwa m'khutu adzadzunjikitsa aphunzitsi monga mwa zilakolako za iwo okha: ndipo adzalubza dala pachoonadi, nadzapatukira kutsata nthano zachabe." Ena mwa anthu awa ndi oona mtima ndi achangu ku chikhulupiriro chao monga mmene amachitira anthu amene amakhulupirira choonadi.

Pa Agalatiya 1:8-9 Paulo ananena kuti, "Koma ngakhale ife, kapena mngelo wochokera Kumwamba, ngati akakulalikireni Uthenga Wabwino wosati umene tidaku-lalikirani ife, akhale wotembereredwa.

*Monga tinanena kale, ndipo ndinenanso tsopano apa, ngati wina akulalikirani Uthenga Wabwino wosati umene mudau-landira, akhale wotembereredwa." Uku ndi kulankhula kwa ndithe ndithe ndithu ndipo ngati pali choti tiphunzire pa ndimeyi, ndicho chakuti zimene m'hristu amakhulupirira zikhazikike ndi kuzikika pa choonadi. Komatu zimenezo ziyanera zizunguliridwe ndi choonadi ndipo zisadutse pa choonadi komanso mpingo usalole kulandira chilichonse chabodza.*



Pa 2 Akorinto 1:12 Paulo akunena za "m'chiyoero ndi kuona mtima kwa Mulungu," Munthu akhoza kukhala oona mtima monga mmene angakwaniritsire pa chikhulupiriro kapena pa zimene akuchita; koma ndi kuona mtima kwa Mulungu kokha kumene kungabweretse chipulumutso mwa iye ndi kumukhazikitsa mwa Mulungu.

Paulo mwiniwake ndi chitsanzo cheni-cheni cha izi. Pa Machitidwe 26:9-10, Paulo akuti, "Inedi ndinayesa ndekha, kuti kundiyenera kuchita zinthu zambiri zotsutsana nalo dzina la Yesu Mnarayo..." Mmene amachita zonsezi

moona mtima ndithu, akanatha kusempavanaugh nacho chipulumutso ngati sakana-dzipereka kwa Khristu namukhulupirira pamene anakumana naye maso ndi maso pa njira yopita ku Damasiko.

Ndiganiza kuti Paulo anakhalanso oona mtima pa choonadi ndi chikhulupiriro cha chikhristukuposa mmene akanakhalira pachipembedzo chake chakale cha Chiyuda ndi zikhulupiriro za makolo ake. Nzosachita kufunsa kuti masiku ano pali anthu amene amachita zinthu moona mtima ndi mwa-changu ndipo amakhala okonzeka kuchita chilichonse ngakhale zinthu zolakwika zimene zimakana mfu-ndo zofunikira za chipulumutso, monga mmene akhristu enieni amakhalira oona mtima pa Khristu ndi choonadi. Kumbukirani kuti si kuona mtima kokha kumene kumafunikira, koma kuona mtima mwa Mulungu ndiye zenizeni.

Tiyeni tiganizirenso zakuti ngati chikhulupiriro cha munthu kaya ndi cha mtundu wotani kapena kuti chili mu zotani malingana ngati chili choyenera ndi chivomereze ka iye pokhapokha ngati akuchita moona mtima, zitatero zikhoza kupangitsa kuti aliyense akhale ndi muyeso wake, komatu Mulungu ali ndi muyeso umodzi ndipo amawaitana anthu onse kuti abwere kwa iye. Pa Aefeso 4:5 amanena kuti pali, "...chikhulupiriro chimodzi,..." Mulungu akuitana okhulupirira onse ku "umodzi wa chikhulupiriro" ndipo wapereka zothandizira kuti ife tonse kuti tilandire zonsezi ngati ife tonse tikhulupirire mu chiphunzitso choona cha Mau a Mulungu.

# Lembetsani Lero!

Yosavuta. Yachangu. Yabwino. Yaulere.

Tipezeni pa intaneti pa [www.thegospeltruth.us](http://www.thegospeltruth.us) kuti mudzitha kulandira kalata yanu yaulere pa intaneti. Mukatero mudalandira uthenga pa email wokudziwitsani za mmene mungachitire kuti muwerenge kalata imene yatulutsidwa kumene.

Lembetsani lero ndipo mugawane ndi anzau.



## Muposa Mtengo Wake

### KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth  
605 Bishops Ct.  
Nixa, MO 65714  
USA

Email:  
[editor@thegospeltruth.us](mailto:editor@thegospeltruth.us)

### CHIYERO KWA AMBUYE

*"Kodi mpheta zisanu sizigulidwa timakobiri tiwiri? Ndipo palibe imodzi ya izo iiwalika pamaso pa Mulungu; komatu ngakhale matsitsi onse a pamutu panu awerengedwa. Musaopa, muposa mtengo wake wa mpheta zambiri"* (Luka 12:6-7).

Panthawi ya Khristu, mpheta ziwiri zimagulidwa ndi kakobiri kamodzi. Mpheta zinai zimagulidwa ndi timakobiri tiwiri ndipo mpheta yachisanuyo imakhala ya basela imene ogulitsawo amaperekwa kuti awakope anthu kuti agule mpheta zinai. Gulani zinai ndipo mulandire imodzi yaulere. Mpheta imodzi inali ngati pafupifupi 6% ya malipiro amene munthu wakumudzi amalandira pa tsiku. Choncho, mpheta zinali zambiri ndiponzo zinali ndi zotchipa mtengo wake.

Yesu anaonetsera chisamaliro cha Mulungu pa kugawana nawo mfundo yakuti Mulungu saona chin-thu chilichonse ngati chopezeka paliponse kapena chotchipa ngati mpheta imodzi – ya chisanu ija. Mulungu amawerengera ndi kusamalira koposa zinthu zimene ena amaziyesa zopanda ntchito. Kodi nanga Mulungu amakonda ndi kusamalira kwambiri munthu aliyense motani? Iye amayang’ana mkatì mwa chigulu cha anthu nasamalira munthu mmodzi. Mulungu amakhuzzidwa ndi kena kalikonse ka moyo wanu: maganizo aliwonse; mmene mumamvera, zimene zimakukhudzani ndi zimene zimakuchitikirani.

Yesu ananena kuti “ngakhale matsitsi onse a pamutu panu awerengedwa.” Mutu wa munthu muli tsitsi pafupifupi 100,000. Mulungu amadziwa ngakhale zazing’ono zokhudza ifeyo. Iye amakhala nafe nthawi zonse popeza kuti ndiye mfumu yathu, mpulumutsi wathu, mnzathu, mthandizi wathu, komanso wotipatsa chisomo. “Musaope” pamene mayesero ndi mavuto afika pa moyo wanu. Mulungu sanakuiwaleni. Iye anawerengera amene amamumvera komanso wosamvera, wolemera ndi wosauka, am-phamvu ndi ofooka, odwala komanso athanzi.

Ndinu a mtengo wake kuposa mpheta zambiri.

-mws

